



Moyo ndi wodzaza ndi mafunso. Mafunso ena ndi aan'gono ndi osafunika, ena ndi mafunso ozama ndipo pali mafunso ena amene ali ofunika kwambiri.

Ngakhale pamene mukuwerenga mau awa, mukhoza kukhala ndi mafunso okhudza thanzi lanu, chuma chanu, ntchito yanu, banja lanu kapena tsogolo lanu.


Koma mwa mafunso onse, mafunso ofunika kwambiri, ndi okhudzana ndi Mulungu ndi chiyanjano chanu ndi lye. Palibe chinthu chofunika mu moyo wa munthu choposa ichi. Thanzi labwino, chuma chokhazikika, ntchito yokhazikika, banja lokhutitsidwa ndi tsogolo labwino zonsezi ndi zinthu zimene anthu afuna. Komatu ngakhale izi ndi zinthu za kanthawi kochepea ndipo kenako zikhala zosafunika pokhapokha moyo wanu uli ndi chiyanjano ndi Mulungu, chiyanjano chodziwika bwino ndi chotsimikizika — chiyanjano chosatha, cha nthawi zonse.

Mu masamba otsatirawa mudzazindikira chifukwa chimene chiyanjano chimenechi ndi chofunika mwansanga kwambiri — ndi momwe chiyanjano chimenechi chimayambira.

Mafunso otsatirawa ndi ozama ndi ofunika kuposa onse amene munthu akhoza kufunsa. Mayankho ake ndi mayankho amene munthu ali yense afuna kudziwa.

Chonde, werengani masamba amenewa mwaluntha ndi mosamalitsa — ndipo ngati ndi kotheka, werengani mobwereza mpaka mutamvetsa.

Uthenga wake ndi wofunika kwambiri woti palibe amene sangafune kumva.



Kuli wina uko?

Ili ndi funso lofunika kwambiri. Ngati Mulungu kulibe, kumufuna-funa ndi chinthu chopanda pake. **Pakuti iye wakudza kwa Mulungu, ayenera kukhulupirira kuti alipo.** ¹ Ngakhale sitingathe kuonetsa kuti Mulungu alipo monga m'mene timachitira polemba masamu, umboni wake woti Mulungu alipo ndi wotsimikizika kwambiri.

Tatiyeni titenge dziko m'mene likhalira. Tikanena kuti zinangochitika mwangozi kuti dziko likhalepo zibweretsa mafunso ambiri — ndipo siziyankhanso funso liri lonse. Izinsu ndi chimodzi-modzi kuganizira kuti kunaphulika bomba lalikulu lomwe linadzetsa kupangidwa kwa dziko monga ena amanenera. Kodi zopangira dzikolo zinachokera kuti? Ngakhale kuombana kwakukulu sikungapange chinthu kopanda kumene zachokera zinthuzo! Maganizo oti anthu anachokera ku zinthu zazing'ono zimene zinasintha nthawi yaitali, kenako anyani ndipo anthu anachokera kwa anyani ndi maganizo amene afalikira kwa anthu ambiri, komanso ndi maganizo opanda mphamvu: kodi kopanda chiri chonse kungachitike chiri chonse? Zingatheke bwanji kuti chinthu chimene kulibe chisinthu ku chinthu chimene chilipo, komanso taonani kudabwitsa kwa chilengedwe ndi moyo wa zinthu zosiyana-siyana zimene ziri m'dziko?²

Maganizo ena onse okhudza chilengedwe ndi opanda mphamvu. Maganizo ogwira mtima ndi awa: **Pachiyambi Mulungu adalenga kumwamba ndi dziko lapansi.** Dziko lathu ili silinakhalepo chifukwa cha mwayi waukulu umene unakhudza zinthu zimene “zinalipo chikhalire”. M'malo mwake, **maiko ndi a mwamba omwe anakonzedwa ndi Mau a Mulungu, kotero kuti zinthu zopenyeka sizinapangidwa zochokera mwa zooneka.** Chilengedwe chinali ndi chiyambi ndipo ndi Mulungu amene anabweretsa chilengedwe. **Ndipo anati Mulungu, ndipo kunatero; analamulira ndipo zinaima nji.**

Izi zikutsimikizidwa ndi ndondomeko yodabwitsa ya chilengedwe ndi mapangidwe a zinthu zimene tizona kuli konse ndi malamulo amene apangitsa kuti dziko lilunzanitsidwe ndi kukhala monga m'mene likhalira, kuyambira pa zinthu zazikulu kwambiri zopezeka m'dziko mpaka zinthu zazing'ono zosaoneka ndi maso athu. Komatu maonekedwe a chinthu amasowa m'misiri ndipo lamulo limasowa wopereka lamulolo - ndipo Mulungu ali zonse! **Mulungu amene analenga dziko lapansi ndi zonse ziri momwemo, Iyeyo, ndiye mwini kumwamba ndi dziko lapansi.**

Koma umboni wamphamvu kwambiri ndi woti: Mulungu mwini analenga munthu mosiyana ndi nyama zonse, munthu ali ndi "makhalidwe"; amasankha mwanzeru, ali ndi chikumbu mtima ndipo amasiyanitsa chabwino ndi choipa. Akhoza kukonda ndi kukhala wachifundo. Pamwamba pa zonse, ali ndi chikhalidwe chofuna kupembedza. Kodi izi anazitenga kuti? Maganizo oti munthu anachokera mwa zinthu zosaoneka ndi maso kapena kuti mwa ngozi zambiri sizingapange munthu wokhala ndi chikhalidwe ndi maganizo otere: **Ndipo Yehova Mulungu anaumba munthu ndi dothi lapansi, nautira mpweya wa moyo m'mphuno mwache; ndipo munthuyo nakhala wamoyo.** Munthu sanapangidwe mwa ngozi ai. Chipangidwe chake **ndi choopsa ndi chodabwitsa.** Mlengi wake ndi amene analenga dziko lapansi ndi kumwamba yemweyo.



¹ Mau omwe awalitsidwa kwambiri achokera mu Buku Lopatulika monga m'mene tasonyezera pa tsamba 32.

² Awa ndi maganizo ozama amene sitingalembe zonse pano. Ngati maganizo oti zinthu zinachokera mu zinthu zosaoneka amakubvutitsani, werengani buku limene lalembedwa mu chingerezi lochedwa 'From Nothing to Nature' ndipo wolembe ndi Prof. E. H. Andrews (Evangelical Press).



Kodi Mulungu akulankhula?

Funso ili ndi lofunika kwambiri. Ife patokha ndife mbuli, zosadziwa Mulungu. **Kodi ukhoza kupeza Mulungu mwa kufunafuna? Ukhoza kupeza Wamphamvuyonse motsindika?** Mulungu ali pamwamba pa maganizo athu ndipo timfuna Iye kuti adziululire yekha kwa ife.


Njira imodzi imene Mulungu wadziulula yekha ndi kupyolera mu chilengedwe. **Zakumwamba zimalalikira ulemerero wa Mulungu; Ndipo thambo lionetsa nchito ya manja ake.** Kukula kwa thambo, kumwamba ndi kulumikizana kwa zonse ndi kukhala bwino popanda chobvuta, kusiyana ndi kukongola kwa zinthu pakuulula zambiri za Mulungu amene anzilenga. Mu chilengedwe Mulungu waonetsa kukula kwa mphamvu yake, kudabwitsa kwa nzeru zake, nzeru zoposa za luntha la maganizo ndi malingiriro ake. **Pakuti chilengedwere dziko lapansi zaoneka bwino zosaoneka zache ndizo mphamvu yache yosatha ndi umulungu wache; popeza zazindikirika ndi zinthu zolengedwa, kuti iwo adzakhale opanda mau akuwiringula.**

Pamene tilankhulana wina ndi nzake, timadalira mau amene tilankhula kuti timvane. Mulungu nayenso amalankhula kwa anthu kupyolera m' mau — mau amene apezeka mu Baibulo. Mau oti “Ambuye ananena”, “Ambuye analumulira”, ndi “Ambuye anati” adabwerezedwa kupyolera zikwi zinai mu chipangano chakale chokha (kubwereza kwa mazana asanu mu mabuku oyambirira asanu a chipangano chakale). Ichi ndi chifukwa chake timati **Chinenero sicinadza ndi chifuniro cha munthu, koma anthu a Mulungu, ogwidwa ndi Mzimu Woyera, analankhula.**

Mu zolemba zonse za anthu, sitiwerenga zaulosi zambiri zolembedwa ndi anthu wonena kuti Mulungu akulankhula mwa iwowo, ndipo patsogolo pake ndi kuona kukwaniritsidwa kwa ulosiwo osasiyana ndi pang'ono pomwe ndi m'mene zinaloseredwa. Munthu sanganene kuti kukwaniritsidwa kwa ulosi umenewu kwangochitika mwa ngozi chifukwa cha kuchuluka kwa zolosedwazo.


Chinanso ndi m'mene Baibulo lasinthira miyoyo ya anthu. Palibe buku lina liri lonse limene liri ndi mphamvu yosintha moyo wa anthu ngati Baibulo. Miyanda miyanda ya anthu, pa zaka zikwi zikwi, atsimikiza pa moyo wao kuti **Malamulo a Yehova ali angwiwo, akubwezera moyo; Mboni za Yehova ziri zokhazikika, zakuwapatsa opusa nzeru; Malangizo a Yehova ali olungama, akukondweretsa mtima: Malamulo a Yehova ali oyoera, akupenyetsa maso.**

Zatha zaka pafupifupi zikwi ziwiri ndipo palibe wina mu nzeru ina iri yonse amene waonetsa poyera umboni wotsimikizika ngakhale mu liu limodzi mu Buku Lopatulika kuti silinena zoonā.³ Izi ziri chonchi chifukwa cha ichi: **Lemba liri lonse adaliuzira Mulungu. Tiwabvomereze mauwo osati ngati mau a anthu, koma monga m'mene ali, Mau a Mulungu.**



³ Ngati muli ndi mafunso okuzunzana okhudzana ndi Baibulo, werengani buku limene lalembedwa mu chingerezi lotchedwa "Nothing but the Truth" lolembedwa ndi Brian H. Edwards (losindikizidwa ndi Evangelical Press).

Kodi Mulungu ali wotani?



Ili ndi funso lodziwikiratu kuti tiyenera kupezana nalo. Kuzindikira kuti Mulungu alipo ndi chinthu chimodzi, ndipo kuzindikira kuti Mulungu amalankhula nafe mu njira zina monga kudzera mu chilengedwe ndi kupyolera mu Mau a mu Buku Lopatulika ndi chinthu chinanso. Koma tiyenera kudziwa zina kuposa apa. Kodi Mulunguyo ali wotani?

Buku Lopatulika litipatsa mayankho abwino ndi omveka bwino funso ili limene liri lofunika kwambiri. M'munsimu talemba mayankho ena.

Mulungu ndi wamoyo. Mulungu si 'chinthu', 'mphamvu' kapena 'chonyengerera'. Amaganizira, amamva ululu, ali wachifundo ndipo amachita mu njira yoonetsa kuti ndi wamoyo, Munthu Wamoyo. Komatu si 'munthu wamba wongokhala kumwamba uko' kapena 'chimunthu china champhamvu'. **Koma Yehova ndiye Mulungu woona; ndiye Mulungu wamoyo, Mfumu yamuyaya.**

Mulungu ali m'modzi mwa atatu. Pali Mulungu woona m'modzi yekha. Atero Mulungu **Ine ndiri woyamba ndi womaliza, ndi popanda ine palibenso Mulungu.** Mulungu wadziulula yekha ngati 'm'modzi mwa atatu' — Atate, Mwana (Yesu Khristu) ndi Mzimu Woyera, ali yense mwa iwo ali mu chidzalo chonse, Mulungu weni -weni. Buku Lopatulika linena za **ulemerero wa Mulungu Atate;** linena kuti **ndipo Mau (Yesu Khristu) ndiye Mulungu;** ndipo linena za **Ambuye, amene ali Mzimu.** Ngakhale pali Mulungu m'modzi, ali mu utatu wake.

Mulungu ndi Mzimu. Alibe msinkhu. Alibe thupi kapena m'maonekedwe oti china chiri chonse chitha kumuona Iye n'kumati ali motere Mulungu. **Mulungu ndiye Mzimu; ndipo omlambira Iye ayenera kumlambira**

mumzimu ndi m'choonadi. Izi zitanthauza kuti Mulungu saoneka ndi maso athu. **Kulibe munthu anaona Mulungu nthawi zonse.** Zitanthauzanso kuti sali womangika pamalo amodzi pa nthawi iri yonse, koma kuti Mulungu ali ponse-ponse nthawi zonse: **Kodi Ine sindidzala kumwamba ndi dziko lapansi? ati Yehova.** Kunena mwa tchu tchu tchu, izi zitanthauza kuti Mulungu amadziwa zonse zochitika pali ponse. Izi ziphatikiza zonse zimene muchita, ndi zimene munena, komanso malingiriro onse amene ali m'maganizo anu.

Mulungu ndi wosatha. Mulungu alibe chiyambi. Mau a Mulungu okha anena kuti, **Inde, kuyambira nthawi yosayamba kufikira nthawi yosatha, Inu ndinu Mulungu.** Panalibe nthawi ina iri yonse imene kunalibe Mulungu ndipo sikudzakhala nthawi imene Mulungu sadzakhhalako. Mulungu ponena za Iye yekha adzifotokoza kuti **amene ali, amene adali, ndi amene alinkudza.** Ndipo akhala chimodzi-modzi nthawi zonse: **Ine Yehova sindisintha.** M'mene Mulungu adali, ali lero ndipo adzakhala nthawi zonse.



Mulungu ndi wokwanira. Cholengedwa china chiri chonse chidalira china chake, kaya munthu kapena zinthu zidalirana, ndipo potsiriza, zonse zidalira Mulungu — koma Mulungu ali wokwanira kwathunthu mwa Iye yekha — wosadalira chilengedwe chake. Akhoza kukhala mwa Iye yekha. **Satumikiridwa ndi manja a anthu, monga wosowa kanthu, popeza Iye mwini apatsa zonse moyo ndi mpweya ndi zinthu zonse.**

Mulungu ndi woyera. Ali wolemekezedwa woyera, woopsya pomyamika. Sitingafanizire china chiri chonse ndi chiyero cha Mulungu. **Palibe wina woyera ngati Yehova** amene alibe choperewera kapena khwinya. Buku Lopatulika linena za Iye kuti, **Inu wa maso osalakwa, osapenya choipa; osakhoza kupenyenera chobvuta.** Ndipo Mulungu uyu, amene ali woyera afuna chiyero kwa aliyense wa ife. Lamulo lake kwa ife ndi ili: **Mukhale oyera, popeza Ine ndine woyera.**

Mulungu ndi wa chilungamo. Buku Lopatulika linena kuti **pakuti Yehova ndiye Mulungu wa chiweruzo** ndi kuti **chilungamo ndi chiweruzo ndiwo maziko a mpando wachifumu wanu.** Mulungu sangokhala mlengi ndi wokhazika zonse; Iyenso ndi woweruza, wopereka mphatso komanso chilango mu nthawi ina iri yonse, ndi chiweruzo chathunthu, chosaperewera ndi chopanda wowiringula kapena kutsutsa.




Mulungu ndi wathunthu. Chidziwitso chake ndi chathunthu. **Ndipo palibe cholengedwa chosaonekera pamaso pache. Koma zonse zonse zikhala za pambalambanda ndi zobvundukuka pamaso pache pa Iye amene tichita naye.** Mulungu adziwa zonse zakumbuyo, zatsopano ndi zakutsogolo, kuphatikiza malingiriro athu, mau athu ndi ntchito zathu. Nzeru zake ndi zokwanira ndi kuposeratu chidziwitso chathu. **Ha! kuya kwache kwa kulemera ndi kwa nzeru ndi kwa kudziwa kwache kwa Mulungu. Osasunthikadi maweruzo ache ndi njira zache nzosalondoleka!**

Mulungu ndi Mbuye. Iye ndi yekhayo ndi woweruza wapamwamba wa chilengedwe chonse, ndipo palibe chimene chichitika popanda ulamuliro

wake. **Chiri chonse chimkonda Yehova achichita, Kumwamba ndi pa dziko lapansi. Palibe ngozi kapena kudabwitsidwa ndi Mulungu.** Alemba mbiri za maiko onse a padziko ndipo **achita zonse monga mwa uphungu wa chifuniro chache.** Mulungu safuna uphungu kapena chilolezo mu chiri chonse chimene asankha kuchita. Ndiponso palibe wina amene angamuletse kuchita chimene afuna kuchita: **ndipo palibe woletsa dzanja lache, kapena wakunena naye, Muchitanji?**

Mulungu ndi wokwanira: Iye ndi wamphamvu yonse. Mwa mau ake mwini anati **taona, ine ndine Yehova, Mulungu wa anthu onse; kodi kuli kanthu kondilaka Ine?** Izitu sizitanthauza kuti Mulungu akhoza kuchita chiri chonse (Iye sanama, kapena kusintha maganizo ake, kapena kulakwitsa, kapena kuchimwa, kapena kudzikana yekha) koma kuti akhoza kuchita chiri chonse afuna kuchita mogwirizana ndi chikhalidwe chake.



Izi ndi zina ndi zina zimene Mulungu waziulula za Iye yekha zoonetsa m'mene aliri ndi chikhalidwe chake kupyolera mu Baibulo. Pali zoonadi zina za Mulungu mu Baibulo (ndipo tidzaona chimodzi mwa izo pa tsamba 22) ngakhale pali zambiri za Iye zimene sitingathe kuzimvetsa. **Amene achita zazikulu ndi zosalondoleka, zinthu zodabwitsa zosawerengeka.** Apa tikuona kuti **Kunena za Wamphamvu yonse, sitingamsanthule** ndipo palibe nzeru ya umunthu kapena kulingirira kumene kungathe kusintha ichi. Izi zisatidabwitse. Ife ngati tingadziwe zonse za Mulungu, ndiye kuti sayenera kulambiridwa ndi ife chifukwa tiri amodzi.

Ndine yani?



Kupanikizika kwa moyo ndi mabvuto a moyo uno kwapangitsa anthu ambiri kuyesa-yesa kufufuza tanthauzo ndi cholinga cha moyo. Taonapo kale zina zotionetsa m'mene Mulungu aliri; nanga bwanji ifeyo? Tiri ndi moyo chifukwa chiyani? Chifukwa chiyani tiri pano? Kodi moyo wa munthu uli ndi tanthauzo kapena cholinga chiri chonse?

Chinthu choyambirira kuchimvetsa ndi choti munthu sanangokhala ai. Munthu alipo osati chifukwa cha kupangidwa mwa ngozi poonkhetsa zonse zofunikira kuti zikhale munthu. Buku Lopatulika litiuza kuti munthu anachita kulengedwa ndi Mulungu wa nzeru komanso Mulungu woyera. **Mulungu ndipo adalenga munthu m'chifanizo chache, m'chifanizo cha Mulungu adamlenga iye; adalenga iwo mwamuna ndi mkazi.** Munthu aposa chinyama chiri chonse chimene chayesetsa kukwezedwa kapena nyani amene waphunzitsidwa zambiri zoti akhoza kuchita ngati munthu. Iye ndi wosiyana ndi nyama zina zonse monga nyama zisiyana ndi masamba ndi monga masamba asiyana ndi miyala yoyengedwa. Poganzira za kukula, munthu ndi wochepa kwambiri poyerekeza ndi dzuwa, mwezi ndi nyenyezi, koma Mulungu wamupatsa munthu malo apadera ndi aulemu mu chilengedwe.

Izi zioneka mu lamulo limodzi limene Mulungu anapereka kwa munthu: **mulamulire pa nsomba za m'nyanja, ndi pa mbalame za mlengalenga, ndi pa zamoyo zonse zakukwawa pa dziko lapansi.** Munthu anakhala nthumwi yomirira Mulungu padziko lapansi, ndi ulamuliro pa zolengedwa zina zonse zamoyo.

chifanizo cha Mulungu' sizitanthauza kuti kukula kwa mapangidwe ake kapena thupi lake ndi chimodzi-modzi ndi Mulungu (taona kale kuti Mulungu alibe thupi kapena maonekedwe a pamaso), kapena kuti munthu ndi mulungu wamng'ono, wokhala ndi zonse zimene Mulungu ali nazo, koma mochepa. Kulengedwa mu chifanizo cha Mulungu kutanthauza kuti munthu analengedwa wauzimu, wanzeru, wamakhalidweake ndi wamoyo mu nthawi zonse, ndi chikhalidwe changwirowiro. Mu njira ina, tikhoza kunena kuti amaonetsera chikhalidwe cha Mulungu changwirowiro ngati m'mene tingamuonere Mulungu mu kalilore.

Chopambana kwambiri ndi choti munthu mokondwa anasankha kumvera malangizo onse a Mulungu ndipo zotsatira zace amakhala moyo wa chiyanjano cheni cheni ndi Mulungu. Munthu sanali kudziderera kapena 'kudzikaikira yekha' pa nthawi imeneyo! Amazidziwa kuti ndi ndani ndi kuti anali pa dziko chifukwa chiyani, ndipo anali pamalo pamene Mulungu anamuika.



Si pokhapo kuti munthu anali wokhutitsidwa ndi wokwaniritsidwa ndi malo amene anali pa dziko lapansi; Mulungu nayenso anakhutitsidwa ndi munthu! Tidziwa izi chifukwa Buku Lopatulika litiuza kuti pamene Mulungu anamaliza nchito yake yolenga zinthu zonse, ndi munthu ngati wapamwamba wa zonse zolengedwa anati, **Ndipo anazona Mulungu zonse zimene anazipanga, ndipo taonani, zinali zabwino ndithu.** Pa nthawi imeneyo mu mbiri, munthu wangwirowiro anakhala mu dziko langwirowiro ndi chiyanjano changwirowiro wina ndi nzake komanso ndi Mulungu.

Si m'mene zinthu ziliri lero ai! Chimene chinachitika ndi chiyani?



Chinalakwika ndi chiyani?

Kuyankha kwa tchu tchu tchu kwa funso limeneli ndi uku: **Chifukwa chache, monga uchimo unalowa m'dziko lapansi mwa munthu m'modzi, ndi imfa mwa uchimo.**

Munthu woyamba wa mwamuna ndi wa mkazi (Adamu ndi Hava) anapatsidwa ufulu wochuluka, komanso chenjezo lamphamvu limodzi: **koma mtengo wakudziwitsa zabwino ndi zoipa usadye umenewo; chifukwa tsiku limene udzadya umenewo udzafa ndithu.** Iyi inali njira yomuyesera munthu ngati angaganizire kumvera Mulungu chifukwa Mulunguyo watero. Koma Satana anamuyesa Hava kuti asakhulupirire ndi kumvera zimene Mulungu ananena, ndipo mkaziyo anatsatira Satana. **Ndipo pamene anaona mkaziyo kuti mtengo unali wabwino kudya, ndi kuti unali wokoma m'maso, mtengo wolakalakika wakupatsa nzeru, anatenga zipatso zache, nadya, napatsanso mwamuna wache amene anali naye, nadya iyenso.**

Pa nthawi imeneyo 'uchimo unalowa mdziko'. Kupyolera mu kusamvera munthu anadzidula yekha kuchoka kwa Mulungu. M'malo mokonda Mulungu, Adamu ndi Hava anayamba kumuopa Mulungu: **ndipo anabisala Adamu ndi mkazi wache pamaso pa Yehova Mulungu pakati pa mitengo ya m'munda.** M'malo mokhala ndi chitsimikizo ndi kulimba mtima ndi chimwemwe, uchimo wao unawapangitsa kukhala amanyazi, olasidwa mu mtima ndi amantha.

Koma Mulungu anati munthu adzafa akadzakana kumumvera, ndipo munthu anafadi. Imfa itanthauza kusiyana ndi Mulungu, ndipo pa nthawi imene munthu anakana kumumvera Mulungu, munthu anadzilekanitsa ndi Mulungu; anafa mu uzimu. Ndipo anayamba kufanso mu thupi, ndipo

tsopano anali ndi moyo wakufa ndi thupi lakufa. Komanso si zokhazo: ana a Adamu ndi Hava anatenga chikhalidwe chokhota ndi chauchimo. Kuchokera pamenepo mpakana lero, monga kuononga madzi kuchokera pa kasupe wake, kuipa kwa uchimo kwayandamira pa mtundu wonse wa Adamu **chotero imfa inafikira anthu onse, chifukwa kuti onse anachimwa.**

Onetsatsani mawu awa ofunika 'onse', amene akuphatikiza tonse wolemba ndi wowerenga tsamba ili. Mwina sitidzaonana pa moyo wa pansu pano, koma tiri nacho chinthu chimodzi tonse — ndife ochimwa ndipo tikufa. **Tikati kuti tiribe uchimo, tidzinyenga tokha ndipo mwa ife mulibe choonadi,** ndipo ngati tinena kuti ife sitikufa tiribe nzeru. Kudzinyenga ndi zinthu za umboni wooneka sikusinthika kanthu.



Mitu ya nyuzipepala zambiri lero, zoonera za kanema ndi nkhani za mawayilesi zitikumbutsa za choonadi choti dziko lasokonezeka. Ndi chinthu chapafupi kutsutsa upandu, kupanda chilungamo, kusowa dongosolo ndi zolakwika za dziko, koma tisanaweruze anthu ena tayasani kudzifunsa ngati muli wa chilungamo ndi wokhala moyo wokondweretsa Mulungu woyera. Kodi inuyo ndinu wokhulupirika kotheratu, wachiyero, wokonda ndi wosangoyang'anira za inu nokha? Mulungu adziwa mayankho anu pa zonsezi — komanso inuyo! **Pakuti onse anachimwa, naperewera pa ulemerero wa Mulungu.** Inu ndinu wochimwa mwa chibadwa, mwa chikhalidwe, mwa kuchita ndi mwa kusankha kwanu, ndipo muyenera kuona mwansanga zoonadi zimenezi — ndi zotsatira zace.



Kodi tchimo ndi loopsya kwambiri?

Matenda akadziwika, ndi chinthu chofunika kufunsa funso ili: ‘Kodi ndi matenda oopsya?’ Ndi chinthu chofunika kwambiri kufunsa funso limeneli pa za matenda auzimu a uchimo. Anthu ambiri akhoza kubvomera monyadira kuti ali ochimwa, chifukwa alibe lingaliro la kutanthauza kwa zimene anena. Amatenga kuchimwa ngati ‘chikhalidwe cha munthu’, kapena amabisala ndi maganizo oti ‘anthu onse amachita izi’. Koma mau onsewa azemba funso leni-leni: kodi uchimo ndi woopsya? Tiyeni tione zimene Buku Lopatulika linena za inuyo ngati wochimwa.

Ndinu woperevera pa chikhalidwe cha umunthu. Izi sizitanthauza kuti ndinu woipitsitsa, kapena kuti mumangokhalira kuchimwa nthawi zonse kotero kuti palibe tchimo limene simunalichite. Izi sizitanthauzanso kuti simungasiyanitse chabwino ndi choipa kapena kuchita zinthu zokondweretsa ndi zothandiza. Koma zitanthauza kuti tchimo lakhudza gawo liri lonse la umunthu ndi chikhalidwe chanu — maganizo, malingiriro, zokonda zanu, chikumbu mtima, magwero a malingiriro ndi kufanizira zinthu. **Mtima ndiwo wonyenga koposa, ndi wosachiritsika.** Tsinde la bvuto lanu si zimene muchita ai koma m’mene muli inuyo! Mumachimwa chifukwa ndinu wochimwa.

Ndinu odetsedwa: Buku lopatulika silinena mophiphiritsa pa ichi: **Pakuti m’kati mwache mwa mitima ya anthu, muturuka maganizo oipa,**

zachiwerewere, zakuba, zakupha, zachigololo, masiro, zoipa, chinyengo, chinyanso, diso loipa, mwano, kudzikuzi, kupusa. Taonani kuti zimene zatchulidwa ziphatikiza maganizo, mau ndi zochita. Izi zionetsa kuti pamaso pa Mulungu, machimo onse ndi ofanana. Ena aganiza kuti kuchimwa ndi zinthu monga ngati kupha, chigololo ndi kuba, koma Buku Lopatulika linena mwachim vekere kuti tiribe ufulu woganizira uchimo mu njira yotere. Uchimo ndi chiri chonse cholephera kufika pa muyeso wamphumphu wa Mulungu. Chiri chonse chimene tinena, tiganiza kapena kuchita chimene chiperewera muyeso wamphumphu ndi tchimo. Tiyeni tione maso ndi maso funso ili: **Ndani anganene, Ndasambitsa mtima wanga, Ndayera opanda chimo?** Mukhoza kutero inu? Ngati ai, ndinu wodetsedwa.

Ndimu osamvera. Buku Lopatulika liphunzitsa kuti **tchimo ndi kusayeruzika,** kugalukira, kusankha kupandukira ulamuliro wa Mulungu ndi malamulo ake. Palibe malamulo oikidwa amene aumiriza munthu kunama, kunena bodza, kukhala ndi maganizo oipa, kapena kuchimwa mu njira ina iri yonse. Munthu amasankha kuchimwa. Mumachita kusankha kuswa malamulo oyer a Mulungu. Mwadala mumakana kumumvera Mulungu, ndipo ichi ndi chinthu choopsya kwambiri, chifukwa **Mulungu ndiye woweruza wolungama, Ndiye Mulungu wakukwiya masiku onse.** Mulungu sadzafewetsa mtima pa uchimo, ndipo mukhoza kutsimikiza kuti palibe tchimo ndi limodzi lomwe limene wina angaganize kuti sadzalangidwa nalo.



Mbali ina ya chiweruzo cha Mulungu pa tchimo ichtika pa moyo uno (ngakhale sitimazindikira nthawi zina). Koma chilango chotsiriza chidzatsanulidwa titafa, pa tsiku la chiweruzo **cotero munthu ali yense wa ife adzadziwerengera mlandu wache kwa Mulungu.**



Ndidzapita kuti ukatha moyo uno?

Pali maganizo ambiri pa mfundo yoti chimachitika ndi chiani pamene timwalira. Ena amanena kuti moyo umatheratu pamene timwalira, ena amati tonsetidzapita kumwamba tikadzamwalira. Ena amati pali malo amene anthu ochimwa amakonzedwa kuti akalowe kumwamba. Maganizo onsewa sagwirizana ndi zimene Baibulo linena.

M'malo mwake, timawerenga zotere: **Ndipo popeza kwaikikatu kwa anthu kufa kamodzi, ndipo atafa, chiweruziro.** Iwo amene ali ndi chiyanjano chabwino ndi Mulungu adzalandiridwa kumwamba, nadzakhala kumeneke moyo wao wonse pamodzi ndi Mulungu mu ulemerero wake. Ena onse **amene adzamva chilango, ndicho chionongeko chosatha chowasiyanitsa ku nkhope ya Ambuye, ndi ku ulemerero wa mphamvu yache.** Mau amene atchulidwa kwambiri mu Buku Lopatulika onena malo awa ndi 'gehena'. Taonani mfundo zinai izi za zoonadi za malo awa:

Alipodi malo ochedwa gehena. Si chinthu 'chongoganiziridwa ndi mpingo'. Buku Lopatulika lafotokoza kambiri - mbiri za gehena kuposa za kumwamba ndipo sasiya china chotipangitsa kukaika za ichi. Linena za **kulangidwa ku gehena ndi kuponyedwa m'gehena.**


Gehena ndi malo oopsya. Alongoledwa mu Buku Lopatulika ngati **malo amazunzo; mng'anjo ya moto; malo a moto wakunyeketsa ndi moto wosazima.** Ndi malo a mazunzo, kuli **kulira ndi kukukuta mano** ndiponso

kulibe kupuma usana ndi usiku. Mau awa ndi mau oopsya, koma ndi mau oona. Amene ali ku gehena adulidwa ku zabwino zonse, otembereredwa ndi Mulungu ndipo otsekereredwa ku kachithandizo ngakhale kochepa kapena chithonhozo chimene chibwera pokhala mwa Mulungu.


Gehena ndi malo otsiriza. Misewu yonse yopita ku gehena ndi yopita mbali imodzi, kotero kuti ukalowa, palibe kutuluka. Pakati pa Gehena ndi kumwamba **pakhazikika phompho lalikulu.** Kuopsya, kusungulumwa ndi kuwawa kwa gehena kwakhazikika osakhala kuti munthu azikonzenso koma kulanga — kulanga kwake kosatha!

Ndi koyenera kukhala ndi gehena. Buku Lopatulika litiuza kuti Mulungu **adzaweruza dziko lokhalamo anthu m'chilungamo,** ndipo ali wolungama potumiza anthu ochimwa ku gehena. Mwa zonse, akuwapatsa zimene anthuwo anasankha. Iwo okana Mulungu pano; Mulungu nayenso adzawakana uko. Anthu amene asankha kukhala moyo wosaopa Mulungu; Mulungu asindikiza chisankho chawo — ku nthawi zonse. Sitingamuimbe mulandu Mulungu kuti alibe chilungamo kapena kuti sanachite bwino!

Tikazindikira zoonadi zoopsya izi, inu muyenera kulingirira mofatsa za funso limene anthu ena mu chipangano chatsopano anafunsidwa: **mudzatha bwanji kuthawa kulanga kwache kwa gehena?**



Kodi chipembedzo chingathandize?



Munthu atchedwa kuti ali wa chipembedzo. Buku la kafukufuku wa chipembedzo ndi chikhalidwe lalemba njira zambiri-mbiri zimene anthu amayesa kukhutitsa chikhumbo cha mtima wao ndi maganizo awo mu zipembedzo. Apembedza dzuwa, mwezi ndi nyenyezi; dziko, motondi madzi; milungu ya mitengo, miyala ndi zitsulo; nsomba, mbalame ndi nyama. Apembedza milungu ndi mizimu yosawerengeka zimene ziri milungu yopanga ndi manja awo ndi maganizo awo okhota khota. Ena ayesapo kupembedza Mulungu woonayu kudzera mu nsembe, kutumikira, kupatula ndi misonkhano yosiyana-siyana. Koma ‘chipembedzo’, chikhale choona mtima bwanji, sichingathe kuthetsa bvuto la uchimo limene munthu ali nalo, pa zifukwa zitatu mwa zifukwa zina zimene ziripo.

Chipembedzo sichikwanitsa mtima wa Mulungu. Chipembedzo ndi njira imene munthu amayesa mwa iye yekha kudzikonza ndi Mulungu; koma kuyesa kwina kuli konse nkosapindulitsa chifukwa pamene munthu amayesa kuti apa ndiye ndayesa ndi polephera komanso posabvomerezeka ndi Mulungu. Buku Lopatulika linenetsa kuti: **zolongama zathu zonse ziri ngati chobvala chodetsedwa.** Mulungu afuna chiyero chonse; chipembedzo chilephera kukwaniritsa zimene Mulungu afuna.

Chipembedzo sichingachotse uchimo. Zabwino zanu sizingachotse zoipa zanu. Ntchito zabwino zanu sizingachotse ntchito zanu zoipa. Ngati munthu ali ndi chiyanjano chabwino ndi Mulungu, ichi **sichichokera kunchito, kuti asadzitamandire munthu ali yense.** Palibe chimene tingayese mu chipembedzo kapena zochita — kupereka dzina la chikhristu, kulandira, kutsimikiza, kubatizidwa, mgonero, kupita ku nyumba ya chipembedzo, kupemphera, zopereka (mphatso), kupereka nthawi mu kutumikira ndi zochita, kuwerenga Buku Lopatulika kapena china chiri chonse — palibe chimene chingachotse ngakhale tchimo limodzi.

Chipembedzo sichingathe kusintha khalidwe la uchimo la munthu. Bvuto si chikhalidwe cha munthu ai. Chikhalidwe ndi chionetsero chabe. Mtima wa bvuto la munthu ndi bvuto la mtima wake, ndipo mwa chikhalidwe mtima wa munthu ndi wonyenga wosachiritsika. Kupita ku nyumba ya chipembedzo ndi kutenga gawo pa zochitika mu chipembedzo zikhoza kukupangitsa kumva bwino, koma sizikupangani inu kukhala wabwino ai. **Adzatulutsa choyera m'chinthu chodetsa ndani? nnena mmodzi yense.**

Zina mwa zochita za chipembedzo zimene tazinenzazi ndi zabwino mwa izo zokha. Mwachitsanzo, ndi chinthu choyenera munthu kupita ku nyumba ya chipembedzo, kuwerenga Mau a Mulungu ndi kupemphera, chifukwa Mulungu watiuza kuchita zinthu zimenezi. Koma musayese ndi pang'ono pomwe kudalira izi kuti zingakuyanjanitseni ndi Mulungu. Ziribe mphamvu yotere; kudalira izi zimangoonjezera uchimo wanu ndi chiweruzo chanu ndi Mulungu.





Kodi yankho lilipo?

Inde, yankho lilipo! — ndipo Mulungu wapereka yankholo. Uthenga wofunika mu Buku Lopatulika unenedwa mwachindunji mu mau awa: **Pakuti Mulungu anakonda dziko lapansi kotero, kuti anapatsa Mwana wache wobadwa yekha, kuti yense wakukhulupirira Iye asatayike, koma akhale nawo moyo wosatha.**

Taona kale kumbuyoku kuti Mulungu wachilungamo ndi woyera ayenera kulanga tchimo. Komanso Buku Lopatulika litiuzanso kuti **Mulungu ndi chikondi.** Ngakhale Mulungu adana ndi tchimo amakonda anthu ochimwa nakhumbira kuti awakhululukire. Koma nanga munthu wochimwa akhululukidwa bwanji mwachilungamo pamene lamulo la Mulungu ligamula kuti munthuyo ayenera kufa mu thupi ndi mu uzimu? Mulungu yekha ndi amene akanatha kutha bvuto limeneli, ndipo analithadi mwa munthu uyu Yesu Khristu. **Atate anatuma Mwana akhale Mpulumutsi wa dziko lapansi.**

Mulungu mwana anakhala munthu potenga chikhalidwe cha umunthu. Ngakhale Yesu analidi munthu, analidinsu Mulungu: Buku Lopatulika linena kuti **pakuti mwa Iye chikhalira chidzalo cha Umulungu m'thupi.** Anakhala Mulungu weni-weni ngati kuti sanakhale munthu; anakhala nthawi yomweyo munthu weni-weni ngati kuti sanakhale Mulungu. Yesu Khristu ndi yekhayo amene anatero ndipo Buku Lopatulika litsimikiza ichi mu njira zambiri. Chiyambi cha kubadwa kwake chinali chodabwitsa: analibe bambu mu thupi koma anabadwa mwa namwali kupyolera mu kuima kwa namwali modabwitsa mwa mphamvu ya Mzimu Woyera. Mau ake anali

odabwitsa: Ndipo **anadabwa ndi chiphunzitso chache; chifukwa mau ache anali ndi ulamuliro**. Zozizwitsa zake zinali zoposa: anayenda-yenda **nachiritsa nthenda zonse ndi kudwala konse mwa anthu**, ndipo mu nthawi zambiri anaukitsanso ngakhale akufa. Khalidwe lake linali lodabwitsa: **anayesedwa m'zonse monga momwe ife tiyesedwa — koma wopanda uchimo** kotero kuti Mulungu Atate akanatha kunena za Iye, **'Uyu ndiye Mwana wanga wokonedwa, mwa Iyeyu ndikondwera.'**

Muonetsetse lingaliro limeneli! Ichi chitanthauza kuti Yesu ngati munthu anasunga lamulo la Mulungu mu gawo liri lonse kotero kuti sanali pansu pa mphoto yake ya uchimo imene ili kufa kawiri. Iye anamangidwa pa mlandu wonamiziridwa, nalamulidwa kuti aphedwe pa umboni wonama, ndipo potsiriza anakhomedwa pamtanda mu Yerusalemu. Komatu imfa yake siinali yonama kapena yochitika mwa ngozi imene sakanatha kuipewa. Zonsezi zinali ndondomeko yoperekedwa **ndi uphungu woikidwa ndi kudziwiratu kwa Mulungu**. Mulungu anatuma Mwana wake pa cholinga chimenechi cholipira mphoto ya uchimo ya imfa, ndipo Yesu mosaumirizidwa analola kubwera. Mu mau ake a Iye yekha, cholinga cha kubwera kwake mu dziko lapansi anati kuti kunali **kupereka moyo wache dipo la anthu ambiri**. Imfa yake, monga moyo wake, inali yapamwamba.

Izi zipangitsa kufunika kwake kuti mumvetse kwambiri chimene chinachitika pamene Yesu anafa, ndiponso kuti imfa yake itanthauza chiani kwa inuyo.





Kodi mtanda ndi wofunika bwanji?


Ziphunzitso zonse za m'Buku Lopatulika ziloza ku imfa ya Yesu Khristu. Uthenga wa Buku Lopatulika sunakhazikike pa moyo wake wa chiyero, kapena ziphunzitso zace zozizwa, kapena zodabwitsa zimene anazichita. Zonsezi ndi zinthu zofunika, koma pamwamba pa zonsezi, Yesu anabwera pa dziko lapansi kudzafera anthu. Chimene chipangitsa imfa yake kukhala yofunika ndi chiyani? Yankho lake ndi loti Iye anafa ngati Wolowa m'malo, Wonyamula tchimo lathu lonse ndiponso Mpulumutsi.

Yesu Wolowa m'malo. Ichi chionetsa chikondi cha Mulungu. Anthu ali ochimwa, opalamula, otaika ndi opanda chiyembekezo pamaso pa chilamulo cha Mulungu, chimene chilamula chilango pa uchimo uli wonse. Kodi anthu angathe kuthawa bwanji mkwiyo wachiyero wa Mulungu? Yankho limene tilipeza mu Buku Lopatulika ndi ili: **Koma Mulungu atsimikiza kwa ife chikondi chache cha mwini yekha m'menemo, kuti pokhala ife chikhalire ochimwa, Khristu adatifera ife.** Ngati mbali ya ndondomeko ya chipulumutso, Mulungu Mwana anadzipereka kutenga malo a anthu ochimwa ndi kulandira chilango choyenerera ndi chachilungamo cha uchimowo. Mwana wa Mulungu wosachimwa analolera kuzunzika ndi kufa m'malo mwathu — **wolungama m'malo mwa osalungama.**

chinyengo china chiri chonse pa imfa ya Khristu. Mphotho ya uchimo inalipiridwa mokwana. Sanangofa mu thupi komanso mu uzimu. Atakhomedwa pa mtanda analira **Mulungu wanga, Mulungu wanga mwandisiyiranji ine?** Pa nthawi yoopsya imeneyo Mulungu Atate anamfulutira Mwana wake wokonedwa, amene anapirira chilango cha kusiyanitsidwa ndi Mulungu. Taonani apa chionetsero cha chiyero cha Mulungu. Machimo onse, tchimo liri lonse, liri ndi chilango — ndipo m'mene Yesu anatenga malo a ochimwa, anatenganso zotsatira za uchimo wao ngati kuti Iyeyo ndi amene anachimwa. Munthu m'modzi amene anakhala moyo wa chiyero anabvutidwa natenga mphoto za imfa zonse ziwiri za wopalamula.

Yesu Mpulumutsi. Ichi chionetsa mphamvu ya Mulungu. Masiku atatu atapita atafa, Yesu **anatsimikizidwa ndi mphamvu kuti ndiye mwana wa Mulungu monga mwa Mzimu wa chiyero, ndi kuuka kwa akufa.** Ndipo Iye **anadzionetsera yekha wamoyo ndi zitsimikizo zambiri,** ndi kuti **sadzafanso; imfa siichitanso ufumu pa Iye.** Pomuukitsanso Yesu kwa akufa, Mulungu atsimikiza mwamphamvu kuti analola imfa ya Yesu m'malo mwa anthu ochimwa ngati malipiro okwana ndi oyenera a uchimo ndiponso ngati maziko amene akhoza kupereka chikhululukiro chaulere kwa ali yense amene mwina anali wopita ku gehena moyo wake wonse.

Koma tsono izi zingachitike bwanji kwa inu? Kodi inuyo mungakhale bwanji angwiro pamaso pa Mulungu? Kodi Khristu angakhale Mpulumutsi wanu bwanji?





Ndingapulumuke bwanji?

Pamene mwawerenga kufikira apa, mukuonadi kuti mufuna kupulumutsidwa? Mukufuna kuti muyanjane ndi Mulungu — kaya zikutengereni zotani kapena zotsatira zake zikhala zotani? Ngati sichoncho, simunamvetse kufunika kwa zinthu zimene mwakhala mukuwerenga. Muyenera kuyambanso kuwerenga, mwachifatso ndi mosamalitsa, kumupempha Mulungu kukuonetsani choonadi cha zimene mukuwerenga.

Ngati Mulungu wakuonetsani chosowa chanu, ndipo mukufunadi kupulumutsidwa, muyenera **kutembenuza mtima kulinga kwa Mulungu, ndi chikhulupiriro cholinga kwa Ambuye wathu Yesu Khristu.**

Muyenera kulapa. Ichi chitanthauza kusintha kwathunthu kuchoka ku uchimo. Malingaliro anu ayenera kusinthika. Muyenera kubvomereza kuti ndinu wochimwa, wopandukira Mulungu woyera ndi wachikondi. Muyenera kusintha mtima wanu — kumva chisoni ndi manyazi ndi kuipa mtima ndi kunyansa kwa uchimo wanu. Ndipo muyenera kubvomera kusiya uchimo ndi kusintha mayendedwe a moyo wanu. Mulungu akulamulira anthu **kuchita nchito zoyenera kutembenuka mtima.** Inu muyenera kuchita chimenechi. Mulungu sadzakhulukira uchimo wanu umene inuyo simukufuna kuusiya. Kulapa ndi kutembenuka ndi kuyenda njira yatsopano, kufuna ndi mtima wonse kukhala moyo wokondweretsa Mulungu.


Muyenera kukhala ndi chikhulupiriro mwa Khristu. Poyambirira, ichi chitanthauza kubvomereza kuti Yesu ndiye **Khristu, Mwana wa Mulungu wamoyo** ndi kuti **Khristu anawafera osapembedza.** Kachiwiri, ichi chitanthauza kuti pokhulupirira mwa mphamvu ndi chikondi chake Khristu

akhoza kutipulumutsa. Kachitatu, chitanthauza kuika chikhulupiro chathu mwa Khristu, kudalira iye yekhaya kuti atiyanjaniitse ndi Mulungu. Kunyada kwanu ndi chikhalidwe chanu cha uchimo chidzachita nkondo kuti mudalire 'ubwino wanu' kapena chipembedzo. Komatu mulibe chisankho. Muyenera kusiya kudalira china chiri chonse ndi kudalira mwa Yesu yekha, amene **akhoza kupulumutsa konse konse iwo akuyandikira kwa Mulungu mwa Iye.**

Ngati Mulungu wakuonetsani chosowa chanu, nakupatsani icho, muyenera kutembenukira kwa Khristu - ndipo muyenera kuchita ichi tsopano! Chofunika kuchita ndi kupemphera momveka kwa iye; pochita izi zimathandiza kumvetsa zimene mukuchita. Bvomerezani kuti ndinu wochimwa, wosochera ndi wopanda chiyembekezo, ndipo ndi mtima wanu wonse pemphani Khristu akupulumutseni, ndi kuti atenge malo oyenera ngati Mbuye wa moyo wanu, kukuthandizani kutembenuka kuchoka ku uchimo ndi kukhala moyo chifukwa cha Iye.



Buku Lopatulika likuti **ngati udzabvomereza m'kamwa mwako Yesu ndiye Ambuye, ndi kukhulupiria mu mtima mwako kuti Mulungu anamuukitsa kwa akufa, udzapulumuka** ndi kuti **pakuti amene ali yense adzaitana pa dzina la Ambuye adzapulumuka.** Ngati inu mwakhulupirira Khristu ngati Mpulumutsi wanu ndi kubvomereza kuti ali Mbuye wanu, mukhoza kuima pa malonjezano amenewa ndi kuwatenga ngati anu anu!




Ngati inu tsopano muika chikhulupiriro chanu mwa Khristu, pali zinthu zambiri zimene mukhoza kukondwera nazo. Mwachitsanzo, tsopano muli mu chiyanjano chabwino ndi Mulungu: Buku Lopatulika linena za ichi kuti 'mwalungamitsidwa' ndipo likuti **Popeza tsono tayedwa olungama ndi chikhulupiriro, tikhala ndi mtendere ndi Mulungu mwa Ambuye wathu Yesu Khristu.** Kudzera mwa Khristu, uchimo wanu wagonjetsedwa; **onse akukhulupirira Iye adzalandira chikhululukiro cha machimo awo mwa dzina lache.** Inu tsopano ndinu chiwalo cha banja la Mulungu: onse okhulupirira Khristu **apatsidwa mphamvu yakukhala ana a Mulungu.** Inu muli otetezedwa mu nthawi yonse: **chifukwa chache tsopano iwo akukhala mwa Khristu Yesu alibe kutsutsidwa.** Mulungu mwini walowa m' moyo mwanu mwa munthu uyu amene ali Mzimu Woyera: **Mzimu wa Iye amene adaukitsa Yesu kwa akufa akhalabe mwa inu.** Kodi sizoonadi zazikulu zimenezi?

Tsopano muyenera kukula mu moyo wanu watsopano wa uzimu. Tikupatsani zinthu zinai zofunikira zimene muyenera kusamalitsa kuzichita:

Kupemphera. Inu tsopano mukhoza kulankhula ndi Mulungu Atate wanu, chinthu chimene simunachitepo chiyambire. Mukhoza kumupembedza Iye, kumuthokoza chifukwa cha ulemere wake, mphamvu zake, chiyero chake ndi chikondi chake. Mukhoza kupempha chikhululukiro tsiku ndi tsiku. Osati kuti iwo amene ali ana a Mulungu ali okhoza mu zonse, koma **ngati tibvomereza machimo athu, ali wokhulupirika ndi wolungama Iye, kuti atikhululukire machimo athu, ndi kutisambitsa kutichotsera chosalungama chiri chonse.** Mukhoza kumuthokoza tsiku liri lonse

chifukwa cha zabwino zimene wakuchitirani. Pali zinthu zambiri zimene mudzafuna kumuthokoza, kuonjezera pa zimene tiri nazo tsiku liri lonse za moyo uno zimene sitingazitenge kuti zimangochitika. Koma mudzafuna kumuthokoza mwapadera chifukwa chokupulumutsani, kukulolani m'banja lake, ndi kukupatsani moyo wosatha. Musazione izi ngati zobvuta kuchita! Mukhoza kupemphanso thandizo, mphamvu ndi chitsogozo m'moyo wanu ndi m'moyo wa ena. Mwapadera, mudzafuna kupempherera anthu ena amene muwadziwa amene ali kutali ndi Mulungu monga m'mene munalili inuyo.

Kuwerenga Buku Lopatulika. Popemphera, mumalankhula ndi Mulungu; mu Buku Lopatulika, Mulungu amalankhula ndi inu. Kotero ndi chinthu chofunika kwambiri kuti muwerenge Buku Lopatulika tsiku ndi tsiku, kuti mudziwe **chokondweretsa Ambuye nchiani**. Pamene muchita izi, mumpemphe kuti akuthandizeni kumvetsa ndi kuzindikira tanthauzo la zimene mukuwerenga ndi kumvera ziphunzitso zace, **kuti mukakule nao kufikira chipulumutso**. Ngati mufuna thandizo kuti muyambe kuphunzira Mau a Mulungu, tilembereni kuti tikutumizireni kabuku kamene talemba pa tsamba 31.



Chiyanjano. Popeza tsopano mwakhala chiwalo cha banja la Mulungu, Iyeyo afuna kuti mudzipezana ndi achimwene ndi alongo anu mwa Ambuye! **osaleka kusunkhana kwanu pamodzi ... komatu tidandaulirane.** Ichi chitanthauza kuti mulumikizane ndi mpingo, choncho tsimikizani kuchita

ichi mwansanga. Kusankha mpingo wabwino si chinthu chapafupi ai, ndipo mudzafuna kupeza mpingo umene umakhulupirira ndi kuphunzitsa zoonadi za M'buku Lopatulika zimene mwakhala mukuwerenga mu kabuku aka. Munthu amene wakupatsani kabuku aka akhoza kukuthandizani. Mu mpingo umene mukhale chiwalo, mudzadziwa zoonjezera za Mulungu; mudzapindulanso kuchokera kwa ena; mudzaphunziranso kufunika kwake kwa chitsogozo cha Mulungu kuti mubatizidwe ndi kulandira mgonero wa Ambuye; ndipo mudzazindikira chimwemwe cha kugawana ndi ena mphatso ndi luntha limene Mulungu wakupatsani. Inu mufuna mpingo, komanso mpingo ufuna inu!

Kutumikira. Uwu udzakhala mwayi wanu **kutumikira Yehova Mulungu wanu ndi mtima wanu wonse ndi moyo wanu wonse.** Nthawi zonse kumbukirani kuti Mulungu atitana ife ndi maitanidwe oyera. Chiyero chikhale choyambirira pa moyo wathu; **pakuti ichi ndi chifuniro cha Mulungu, chiyeretso chanu.** Kotero, funani kugwiritsa ntchito mphatso zanu mu utumiki wa Mulungu; kumbukirani kuti **anatilenga mwa Khristu Yesu kuchita nchito zabwino.** Potsiriza, khalani tcheru kuti musataye mwayi wowauza ena **zinthu zazikulu anakuchitirani Ambuye.** Kuwauza ena za Yesu si ntchito yokhayo ya iwo okhulupirira Yesu, ndi yopatsa chisangalatso ndi mpumulo kwa iwo oyichita!

Kuyambira tsopano, yesani kukhala moyo kotero kuti mbali iri yonse ya moyo wanu **ikalalikire zoposazo za Iye amene anakuitanani muturuke mundima, mulowe kuunika kwache kodabwitsa!**

